*Kodi ndingagwiritse ntchito PrEP limodzi ndi njira za kulera?*

Inde, mungathe kugwiritsa ntchito PrEP pamene mukutenga njira za kulera.

*Kodi ndingagawane PrEP ndi anthu ena kapena okondedwa wanga?*

Sikoyenera kugawana PrEP ndi wina. Kugwiritsa ntchito PrEP wa ena kungathe kubweretsa zotsatira zoipa za mankhwalawo, kupangitsa kuti mankhwalawo asagwire ntchito moyenera komanso kuti mzanuyo akhale ndi mankhwala operewera.

*Kodi munthu amene ali ndi HIV angamweso PrEP?*

PrEP sangagwiritsidwe ntchito ngati mankhwala otalikitsa moyo a ma ARV. Anthu amene ali ndi HIV amayenera kumwa ma ARV opelekedwa ndi azaumoyo malingana ndi zofunika zawo.

**KODI PrEP ALI NDI MAVUTO ENA ALI ONSE?**

Anthu ena akayamba kumwa PrEP, amatha kukhala ndi zotsatira monga izi; kumva mseru, kupweteka kwa mutu (litsipa), kumva kutopa, kutsegula m'mimba, kukhumudwa, kusanza, kutuluka ziwengo, kuvutika kupeza tulo ndi kusowa kwa chilakolako cha chakudya.

**KOMA ZOTSATIRAZI ZIMATHA PAKAPITA SABATA ZOCHEPA KWA ANTHU AMBIRI.**

## *PrEP amagwira ntchito bwino akagwiritsidwa ntchito limodzi ndi njira zina zopewera HIV. PrEP sateteza ku matenda ena opatsirana pogonana komanso mimba.*

*Kodi pamene ndikumwa PrEP, ndingathe kusiya kugwiritsa ntchito makondomu pogonana?*

PrEP ndi njira yoonjezera podziteteza ku HIV ndipo iyenera kugwiritsidwa ntchito pamodzi ndi njira zina monga makondomu. Kugwiritsa ntchito makondomu ndi njira yopambana yopewera HIV. Makondomu amateteza ku matenda ena opatsirana pogonana komanso kupewa mimba ngati akugwiritsidwa ntchito mwandondomeko.

*Kodi PrEP ndi oyenera kwa ine?*

PrEP ndi njira yopamba yodzitetezera ku HIV makamaka kwa anthu amene ali pa chiopsezo chachikulu chotenga HIV. Dziwani kuti azaumoyo adzakuwunikirani ngati kuli koyenera kuti muyambe kumwa PrEP.

*Kodi PrEP amapezeka kuti?*

Pakadali pano m'Malawi muno PrEP amapezeka m'zipatala zokhazikika za boma ndi zamishoni. Mukafuna kumva zambiri, kumanani ndi azaumoyo amene ali pafupi kapena chipatala china chiri chonse chokhazikika.

USAID FROM THE AMERICAN PEOPLE
PEPFAR
HIV Prevention Market Manager
AVAC
fhi360 THE SCIENCE OF IMPROVING LIVES
LIGHTHOUSE




# ZOMWE AMBIRI AMAFUNA KUDZIWA ZOKHUDZA

# PrEP

*PrEP ndi njira ina yoonjezera pa njira zodzitetezela ku HIV kwa anthu amene alibe. PrEP ayenera kumwedwa tsiku ndi tsiku.*




## *Kodi PrEP amagwira ntchito bwanji?*

Anthu amene alibe HIV ndipo akumwa PrEP mwandondomeko amachepetsa chiopsezo chotenga HIV.

*Kodi pali kusiyana kotani pakati pa PrEP, PEP ndi ART?*
Njira zonse zitatu zili ndi ma ARV koma ndi ophatikizidwa mosiyana ndiponso zimagwira ntchito mosiyana:

- **PrEP** amamwedwa ndi anthu okhawo amene alibe HIV ndipo ali pa chiopsezo chachikulu chotenga HIV.
- **PEP** ndi mankhwala amene amamwedwa pasanadutse masiku atatu ndipo amateteza munthu kuti asatenge HIV pamene waikidwa kale pachiopsezo chotenga HIV ngati kugwiliridwa, ndipo amamwedwa kwa masiku 28.
- **ARV** ndi mankhwala otalikitsa moyo amene amaonjezera chitetezo mthupi amene amaperekedwa kwa munthu amene ali ndi HIV.

# PrEP NDI NJIRA YA ANTHU OKHAWO AMENE ALIBE HIV.

## *PrEP ndi oyenera kwa anthu amene ali pa chiopsezo chachikulu chotenga HIV.*

*Kodi ndikuyenera kumwa PrEP motani?*
Mukuyenera kumwa PrEP kamodzi pa tsiku, pa nthawi yomwe yomweyo tsiku lirilonse.

*Kodi PrEP ali ndi vuto?*

PrEP alibe vuto. PrEP angathe kumwedwa ndi munthu amene amamwa mowa, mankhwala ena komanso amene akutenga njira zolera.

*Kodi pamatenga nthawi yayitali bwanji kuti PrEP ayambe kugwira bwino ntchito mthupi?*

PrEP ayenera kumwedwa tsiku lirilonse kwa masiku 21 kuti ayambe kugwira bwino ntchito mthupi!

*Kodi ndipange chani ngati ndayiwala kumwa mankhwala nthawi yoyenera?*

Ngati munayiwala kumwa mankhwala, imwani nthawi yomwe mwakumbukirayo, ndipo pitirizani kumwa masiku enawo mwandondomeko.

**Ngati mukufuna kudziwa zambiri za PrEP, afunseni azachipatala mdela lanu, kapena imbani foni pa 169 (Lighthouse call centre) mwaulere**

*Ngati ndikumwa PrEP, kodi ndiyenera kumwa PrEP kwa moyo wanga wonse?*

Ayi. Muyenera kumwa PrEP kwa masiku wonse amene mukuona kuti muli pa chiopsezo chotenga HIV. Kumanani ndi wa chipatala pa nthawi imene mukuona kuti simuli pa chiopsezo chotenga HIV kuti mudziwe za m'mene mungasiyire kumwa PrEP.

*Ndipange chani ngati nditafuna kusiya kumwa PrEP*

Ngati mwapanga chiganizo chosiya kumwa PrEP, kambiranani ndi wa zachipatala kuti mudziwe za nthawi yomwe mungathe kusiya kumwa mankhwalawa.

*Kodi PrEP amatetezanso ku matenda ena?*

Ayi. PrEP amateteza kutenga HIV basi. PrEP samateteza kutenga mimba komanso ku matenda ena ali onse opatsirana pogonana.

*Kodi PrEP ndingamwe usiku umodzi okha ndikukhala otetezeka?*

Ayi. Muyenera kumwa PrEP kamodzi pa tsiku kwa masiku osachepera 21, kufikira atayamba kugwira ntchito mthupi kuti mukhale otetezeka ku HIV.

## DZIWANI KUTI...

***"...ndi kuchipatala kokha komwe angakuuzeni kuti muyambe kumwa PrEP".***